

KUKONDWERERA CHIYERO



MLOZO WA KUPEMPHERA NDI KUSALA KUDYA

Mpingo Wa Nazarene – Chigawo Cha Africa

www.africanazarene.org

“Ndipo Yoswa ananena kwa anthu,
Mudzipatule, pakuti mawa Yehova
adzachita zodabwiza pakati pa inu.”
Yoswa 3:5

KUUNIKIRA

Chaka cha 2012 chakhazikitsidwa kukhala chaka chokondwerera chiyero! Kukhazikika kwathu koyamba kukhala kwa nyengo yakusala kudya ndikumphera, kumene kudzayambe pa Lachitatu Laphulusa pa, 22 February 2012 ndipo idzafika pampondachimera Lamulungu Loyera pa, 8 April 2012. Nyengo imeneyi imadziwika ndi ambiri ngati nyengo ya Lenti imene idzakumbukilike ndi nthawi yakudziikiza kwa munthu aliyense payekha mmanja mwa Mulungu podzikonzekeretsa ku ‘mivumbi ya madalitso’.

“Yehova, ndinamva mbiri yanu ndi mantha; Yehova, tsitsimutsani ntchito yanu pakati pa zaka Pakati pa zaka muzidziwitse; pamkwiyo mukumbukile chifundo.” (Habakuku 3:2).

Nthawi yakusala kudya ndi kupemphera ndi nthawi imene tingathe kupempha Atate wathu wakumwamba kuti abukitse njala komanso kukhumba kwa chiyero munjira zodabwitsa mwa ife mumpingo wathu wonse wa Nazarene muno mu Africa; ndi nyengo yopempha Mulungu kuyatsa moto wachitsitsimutso komanso mivumbi ya madalitso kwa Anthu ake. Iyi ndi nthawi yopempha kutsitsimuka pachiyero ndikulola Mzimu Woyera kutitsuka ndikutipanga kukhala zida zakholo la lalikulu. Iyi ikhala nthawi yokonzekera kukondwerera mfundo zachiyero kuyambira Lamulungu Loyera pa 08

April 2012 mpaka pa Lamulungu la Pentecoste pa 27 May 2012.

Kaundulayu, wakonzedwa kuti athandize mipingo ya Nazarene payokha, pamene akukonzekera nthawi yakudzipatula kwa Mulungu.

- Pemphero la kutsitsimuka pa chiyero.
 - Kulimbikitsa pemphero lapagulu
 - Kalendala ya ndondomeko ya pemphero
 - Kuyenda mpemphero
 - Ola limene limasintha dziko lapansi
 - Chitsanzo chamsonkhano wapemphero.
 - Phwando lapemphero komanso chitsitsimutso cha chiyero
- Kusalira Chitsimutso cha Chiyero
 - Kalendala lapemphero lamasiku 47 kuyambira nyengo ya Lenti Lachitatu mpaka Lamulungu Loyera komanso maganizo azinthu zochitika kumpingo wanu. Mamembala ampingo achite nawo pazochitika Zokondwerera Chiyero panthawi yakusala kudya ndi kupemphera.
 - Dongosolo lomveka bwino lazochitika panthawiyi

Pemphero la Chitsitsimutso

Kodi pemphero ndi chiyani?

Pemphero ndi kulumikizana ndi Mulungu. Izi zimakhudzanso kuyankhula ndi Mulungu komanso kumva kumayankho Ake. Pemphero ndikuitana kwa ubale wamphamvu ndi Atate wathu wakumwamba. Ubalewu umatsimikizira zakuti Mulungu adatikonda koposa kotero adatuma Mwana wake mmodzi yekhayo

kuti adzatifere pamtanda chifukwa chamachimo athu. . Pemphero ndi kuvomera ku chikondicho pofika kufupi ndi Mulungu komanso kukhala ndi nthawi ndi Mlengi wathu. (Yohane 15:9).

Kodi Tingapemphere motani?

- Sankhani nthawi ndi malo apemphero (Danieli 6:10)
- Khalani ndi mtima oona (Ahebri 10:22)
- Pempherani ndi chikhulupiro (Mateyu 21:22; Yakobo 1:6)
- Pempherani Mdzina la Yesu (Yohane 14:13-14)

Magawo Ena A Pemphero:

- Kupembedza ndi kuyamika (Masalimo 95:1-6; 1 Mbiri 29:11-13)
- Kuthokoza (Masalimo 107:1; Akolose 1:3)
- Kulapa machimo (Mateyu 6:12-13; 1 Yohane 1:9)
- Kupempha zosowa zathu – kupempha Mulungu kuti akumane ndi zosowa zathu. (Mateyu 6:9-13; Yakobo 1:5)
- Kupempherera Ena (Akolose 1:3-12; Yakobo 5:13-16)

Kupempherera Kutsitsimuka pa Chiyero Pawekha

Mapemphero a mfumu Davide akutiphunzutsa zakufunika kwa pemphero lachiyero pawekha:

- Davide adapempha Mulungu kuti amusanthule mumtima ndikupeza machimo obisika (Masalimo 139:23-24)

- Iye adalapa machimo Ake napempha chikhululukiro cha machimo Ake. (Masalimo 51:3-5)
- Iye Adapempha Mulungu kuti ayeretse machimo Ake (Masalimo 51:7)
- Iye adapempha Mulungu kuti abukitse mzimu wokhazikika mwa iye ndipo kuti Mulungu asamulande Davide Mzimu Woyera. (Masalimo 51:10-11)
- Adapempha Mulungu kuti amuchotsere kutsutsika ndi chikumbumtima choipa. (Masalimo 51:14)
- Iye adavomereza kuti Mulungu amayankha mzimu wosweka ndi wolapadi. (Masalimo 51:17)
- Iye adakondwera ndi kulimba mtima pamene Mulungu adayankha mapemphero Ake. (Masalimo 51:18-19)

Kupempherera Chitsitsimutso Chapagulu Pachiyero

Musamalitse izi pamene mukupempherera chiyero chapagulu:

- Mulungu amapeza mipingo imene ili yofunda kuti ndichidetso pamaso pake (Chivumbulutso 3:16)
- Mulungu akufuna kuti mipingo yathu itsitsimuke (Chivumbulutso 2:4-6)
- Mulungu Akufunitsitsa kutipatsa Mzimu Wake Woyera (Luka 11:13)
- Tayani mafano ndi zotchinga zonse (Mateyu 4:8-10; Akolose 3:8-10)

Kodi Tipemphere zotani

- Pempherani kuti Mulungu akhazikitse mzimu wakusweka ndi wogonja (Yesaya 57:15; Yakobo 4:6)
- Pemphererani kumvetsetsa kozama komanso kukhumba chiyero (Yesaya 6:1-5)
- Pempherani kuti Mulungu aonetse machimo obisika mkati mwathu (Masalimo 19:12-14)
- Pemphani njala ya Mawu a Mulungu komanso moyo wofuna kumvera Mulungu (Masalimo 119:97,103; 1 Yohane 2:3-6)
- Pemphererani Abusa komanso Alaliki kuti azilalikira Mawu a Mulungu mwamphamvu komanso modzipereka (1 Corinthians 2:1-4)
- Pempherani kuti okhulupirira akhale ndi chikondi chozama pa Yesu Khristu (Matthew 22:37-38)
- Pemphererani kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera (Luka 11:13; Machitidwe 1:8)

Malonjezo A Mulungu

- Mulungu adzachiritisa dziko lathu (2 Mbiri 7:13-14)
- Mulungu adzatiyankha ngati tipempha muchifuniro chake. (1 Yohane 5:14)
- Mulungu adzatumiza Mzimu wake ngati titapempha (Yoweli 2:28)
- Mulungu adzatipatsa chigonjetso (Aroma 8:37-39)

Pemphero la Gulu Komanso Mfundo Zokhazikikapo ndi Kalendala ya Pemphero

Mpingo wonse udzipereke kukusala kudya ndi kupemphera pokhudzana ndi kutsitsimuka kwa chiyero komanso panthawi yonse imene yaikidwa kale. Poonjezerapo, sabata iliyonse tidzapempherera gulu lina lake mumpingo. Mkati mwasabata, gulu losankhidwalo, libwere pamodzi, kupemphera, kuphunzira mwapadera pokhudzana ndi kusala kudya komanso kupemphera komanso kulimbikitsana wina ndi mzake.

- Sabata loyamba: Amayi
- Sabata lachiwiri: Abambo
- Sabata lachitatu: Achinyamata okulirapo
- Sabata lachinayi: Achinyamata
- Sabata lachisanu: Ana
- Sabata lachisanu ndi chimodzi: Mpingo wonse upemphere pamodzi.

Sabata iliyonse, kalendala yapemphero yalembedwa mzere pokhudzana ndi pemphero lapadera muchigawo chachikulu champingo komanso dera la Africa ndi dziko lonse pamavuto amene alipo lero lino. Gwiritsani ntchito kalendala yapemphero pokonza mapemphero akusala kudya ndi kupemphera. Kumbukirani kuti pempho loyamba panthawiyi ndilakuti Chiyero chipezekenso pakati pa mpingo komanso anthu onse a mu Africa muno.

Kuyenda Mpemphero¹

Kodi Kuyenda Mpemphero ndi Chiyani?

“Kuyenda Mpemphero kutanthauza kupempherera Madera osiyanasiyana amene inu mukufuna kuti Mulungu akuyankheni.” (Kodi Yesu akadapempherera chiyani”, lokonzedwa ndi a Way Makers)

Ili ndi pemphero lofunsa Mulungu mumadera amene mukadafuna kuti Mulungu akuthandizeni. Cholinga chapempheroli ndikulunjika kwa anthu amdera lanu amene mukufuna kuti Mulungu alowererepo.

Kodi Limagwira Ntchito Bwanji?

Kuyenda mpemphero ndiyenda pawekha komanso pagulu pamalo ena amene mukufuna kuti Mulungu ayankhe pazosowa zamalowo. Zimathandiza kuti mulunjike mupemphero pazosowa zadera limene muli.

Kuyenda Mpemphero Ndikupemphera Mudera Limene Lili ndi Zosowa:

- Kuyenda mpemphero ndikupempherera zosowa za Anthu ena.
- Kuyenda mpemphero ndikupempherera Anthu zosowa zawo pamene muli pafupi nawo kuti mudziwe zosowa zawo:
- Kuyenda mpemphero kumathandizira kuti mudziwe zosoweka za anthu ndikuziikiza mmanja mwa Mulungu. Zimene mukumva, kuona komanso kununkhiza zimakuthandizani kupembedzera wena.

¹ *Nkhani zina zokhudza kuyenda mpemphero zapezeka chifukwa cha a Bob Tremaine, mkulu wamishoni , Parker-Palo Pinto Association*

Kuyenda Mpemphero Ndikupemphera mwa Chidziwitso:


- Ndi chidziwitso chakuvomera kuitana. Chimene ukuchipempherera chimakhala pandunji pako
- Ndi chidziwitso chofufuzidwa bwino. Uku ndikupemphera kodziwa malo komanso mbiri yadera imene mukuipemphererayo. Zoyenera kupemphera ndikupempha Mulungu kuti atidziwitse zoyenera kupemphera pazosowa za anthu. Mzimu Woyera ayenera kutitsogolera pamene tikupemphera.

Kodi Tingachite Bwanji Pemphero Loyendayenda:

1. Mupemphere ndi Mzanu kapena gulu
2. Pempherani ndi cholinga – Chokhumba cha Mulungu
3. Pempherani Mawu a Mulungu – pempherani molunjika ku malonjezo a Mulungu osati mavuto anu
4. Pempherani Mu Mzimu wa Mulungu
5. Mvetserani ndi kuyembekezera kwa Mulungu

Ola Limene Limasintha Dziko Lapansi²

Gudumu lapemphero ndilotheandiza kulunjika papemphero. Likugawa ola limodzi mumphindi zisanu zapemphero. Pakatha mphindi zisanu, sinthani mtundu wapemphero lanu. Izi zikuthandizani kulunjika papemphero lakutsitsimuka pachiyero cha mpingo muno mu Africa.



² Chithunzichi adajambula ndi a Dick Eastman, amene adayambitsa sukulu yapemphero ya Change the World School of Prayer

Chitsanzo cha Msonkhano wa Pemphero

Msonkhano Wapemphero ndi umene mumaitana mipingo ina, atsogoleri, mafumu ndipo iwo amakhala ndi nthawi yopembedzera mavuto amene akuchitika mudera lawo. Kubwera pamodzi kupempherera zinthu zofunika m'dera, pemphero lalikulu limakhala kufuna machitachita a Mzimu Woyera

Ndondomeko ya Zochitika:

A. Kulandira Anthu

1. Masalimo 42:1-2; 84:1-2; 10-11; 133:1-3
2. Kuwauza zochita
3. Pemphero lakuzikonzeke: magulu a anthu Atatu. Aliyense anene zazosowa zake komanso zothodwetsa kenako alunjike kuzosowa zadera kapena dziko lawo
4. Kuyamika: Masalimo 132
5. Nyimbo zoyamika

B. Kulapa, kudzikhuthula komanso kudzipatulira kwa Mulungu

Vesi Yoweli 2: 12-14

1. Funsani Ena kupempherera chitsogozo, chitetezo ndi kupezeka kwa Ulemerero wa Mulungu
2. Nyimbo zoyamika
3. Werengani Yakobo 4:8-10. Aliyense akhale ndi nthawi yodzisanthula mmoyo wake wauzimu mpemphero.

C. Pemphero lazosoweka zapadera mudera lanu

Vesi e: 2 Mbiri 7:14

1. Itanani atsogoleri adera lanu ndipo mupempherere zinthu zofunika mdera lanu.
2. Werengani Yoweli 2:28. Pemphererani kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera mdera lanu.

D. Timagulu Tapemphero

1. Sonkhanitsani Abambo pamodzi komanso Amayi pamodzi
2. Uzanani zosowa za aliyense. Abusanso amavutika chifukwa chakutsutsidwa, mpikisano, ulesi pakati pa mamembala komanso kuopa kulephera. Musakambirane zopempherera panthawiyi.
3. Zungulirani magulu ndipo munthu mmodzi apempherere munthu wakumanzere kapena kumanja mpaka aliyense akhale ndi mpata wopemphera komanso kupemphereredwa

E. Pemphero Losuntha Mapiri

Vesi: Yereimiya 33:1-11

1. Pemphererani mabanja: makolo/agogo. Pemphererani Ana otayika
2. Pemphererani kuti mabanja atetezedwe ndikubwezeretsedwanso, kulapa komanso kusintha khalidwe:
3. Pemphererani kuti mipingo yonse, ikhale nyumba zapemphero kwa akulu ampingo ndi atsogoleri komanso akhristu onse

F. Chitsitsimutso, Kukonzedwanso

Vesi: Machitidwe 3:19; Ezekieli 37; Masalimo 85:6

1. Pemphererani mavesi onena za chitsitsimutso, kukonzedwanso komanso mphamvu ya Mzimu Woyera

2. Itanani Atsogolei a mtsogolo amene sadafike zaka 40 kuti afike kutsogolo nagwade ndipo pemphero la kutsukidwa lichitike

G. Mapemphero a kuthokoza komanso kuyamika

Mavesi: 1 Mbiri 29:11-13, Masalimo 95:1-6, Masalimo 100

1. Khalani mmagulu a anthu atatu. Thokozani Mulungu pa zimene wachita pamasiku komanso maola apitawo. Onjezerani mapemphero okhudza mawu Mulungu olonjeza zachiyembekezo pamiyoyo yanu

Zochitika Zapemphero Komanso Kuyamika

Iyi ndi nthawi imene mpingo umafika pamodzi kuwerenga mawu, kuimba nyimbo, kuchitira umboni pokhudzana ndi mapemphero amene ayankhidwa ndi Mulungu komanso kulimbikitsana wina ndi mzake.

Pologalamu iyenera kukonzekeredwa bwino tsikuli lisadafike.

Anthu agawane zochita kuti dongosolo liyende bwino.

Chitsanzo cha phwando la pemphero ndikuyamika lili mmunsimu. Komabe mungathe kuiisinha pologalamu malingana ndi mmene mukuonera.

Chitsanzo chamsonkhano wa pemphero ndi kuyamika

- *Gawani pologamuyi kwa mtsogoleli komanso anthu obwera kumwambowu nthawi isadafike.*
- *Sankhani atsogoleli ambiri.*
- *Tsatirani mapemphero ali pansywa.*
- *Chonde werengani mavesi onse achokere mu Buku Lopatulika.*

Mbusa kapena wotsogolera chipembedzo:
Takulandirani kunyumba yamapemphero yamafuko onse. “Nyumba yanga idzachedwa nyumba yakupempheramo anthu amitundu yonse.”. (Marko 11:17). Chonde tiyeni tiime ndi kugwirizana m'mawu anthu mu kuimba nyimbo zolambira pamodzi.

Mtsogoleli wamapemphero: Nyimbo zotamanda Mulungu — mphindi 15:
Mtundu wina wanyimbo: Tidzamtamanda Yawe, Mwayenera matamando;

Mapemphero kwa kupembedzera ndi kutamanda Mtsogoleli Woyamba: Werengani Masalimo 96

Kuimba limodzi: Haleluya, Hosana

Kupemphera limodzi aliyense payekha. Mapemphero ake akhale othokoza ndikuyamika

Mapemphero akudzisanthula komanso kulapa Mtsogoleli wachiwiri: Werengani 2 Akorinto 7:1

Kuimba limodzi: Kufuna kwanu kuchitidwe kapena Ndaperekatu zanga zonse

Chonde, gwadani panokha kuti mukhale ndi nthawi yakulapa komanso kupemphera

Pemphero lakutsitsimuka pachiyero.

Mtsogoleli wachitatu. Werengani Habakuku 3:2

Imbani nyimbo pamodzi: Mbuye wondipulumutsa.

Khalani mumagaulu a anthu atatu kapena asanu ndikupempherera kutsitsimuka pamoyo wachiyo mumpingo wathu muno mu dera lalikulu la Africa.

Pemphero **Lakupembedzera**
Mtsogoleli wachinayi: Werengani Zakariya 4:6

Imbani limodzi: Ndifuna kuthandiza ofoka No. 141

Pempherani mumagulu anu aja ndipo mupempherere
atsogoleli ampingo

Pemphero **lawanthu** **ochimwa** **kapena**
osapulumsidwa
Mtsogoleri wachisanu werengani Masalimo 2:7-8

Imbani limodzi: Tumizani Mzimu wanu

Lirani pamodzi mpemphero chifukwa cha amene
samudziwa Yesu ngati mpulumutsi wawo.

Pemphero **lamabanja**
Mtsogoleli wachisanu ndi chimodzi: werengani
Genesis 18:19; Deuteronomo 6:6

Kupempherera mabanja: Wamoyo Yesu

Khalani anthu awiri awiri ndikupemphereranso mabanja
komanso mudzipempherere nokha.

Mapemphero **amachiritso**
Mtsogoleli wachisanu ndi chiwiri: Werengani Eksodo
15:26b

Imbani nyimbo limodzi: Ikhale yokhudza Mulungu
wochiza nthenda

Ndikuitana amene ali ndi vuto lanthenda ina iliyonse
afike kutsogolo ndipo ena awapempherere.

Mapemphero **Othokoza**
Mtsogoleri wachisanu nchimodzi: Werengani
Masalimo 100

Imbani limodzi: Kwa Mulungu kukhale ulemerero

Imbani limodzi nyimbo yoyamika ndi kukweza Mulungu

Pemphero la zigawo zina zazikulu (Africa Fields) ndi chigawo chadera la Africa (Africa Region) Mtsogoleli woyamba:

Tsopano tipempherera zigawo zina zazikulu zimene zilipo 7 muno mu Africa. Tiyanba ndi chigawo champingo chapakati mu Africa mtsogleri wathu ndi M'busa Paul Mtambo komanso chakummawa. Mtsogleri wathu muchigawo chapakati ndi Mbusa. Ndipo Mbusa Don Gardner ndi amene akuyang'anira kumaiko akumawa.

Ndipemphe kuti tonse tiime. Tiwerenge Masalimo 96:2-3 limodzi komanso zilembedwe pakhoma ngati nkotheke: "Myimbireni Yehova, lemekezani dzina lache; Lalikani chipulumutso chache tsiku ndi tsiku. Fotokozerani ulemmerero wache kwa amitundu; zodabwiza zace mwa mitundu yonse ya anthu" (Masalimo 96:2-3).

Ndikulimbikitsa anthu amene ali kudzanja langa lamanzere kuti apempherere Abusa Paul Mtambo, ma DS onse komanso abusa awo m'magulu. Amene ali kumanzere kwanga apempherere Mbusa Don Gardner, ma DS awo komanso Abusa onse.

Pemphererani mitu imene ikuyendetsa ma Field onse monga: onetserani kupezeka kwa Mulungu, kulalikira Uthenga Wabwino, chiyero, chitukuko cha mpingo, zigawo zonse ndi atsogoleli Ake, kukula koyenera, kutukula utumiki, kudzipereka mwaunsembe, komanso kukula koonza muuzimu.

Tsopano, itanani magulu aang'ono kupemphera kwa mphindi ziwiri. Pamene nyimbo zayamba, tsekani ndi pemphero.

Imbani: Awa ndi masiku a Eliya kapena nyimbo ina iliyonse yachitsitsimutso

Mtsogoleli wachiwiri: Tikupitliza kupempherera ma Field amaiko a Ethiopia, Sudan, Eritrea komanso Field ya Apwitikizi (Lusophone). Mkulu wa Horn of Africa Field ndi Mbusa Ermias Choliye ndipo Mkulu wa Lusophone Field ndi a Dr. Paul Sueia.

Ndipemphe kuti tonse tiime. Tiwerenge Masalimo 22:27-28 zilembedwe pakhoma “Malekezero onse adziko lapansi adzakumbukira natembenukira kwa Yehova; Ndipo mafuko onse amitundu adzagwadira pamaso panu” (Masalimo 22:27-28).

Ndikulimbikitsa anthu onse adzanja langa lakumanja apempherere Horn of Africa Field ndi Mbusa Choliye, ma DS, Abusa onse ndipo adzanja lakumanzere apemphere Field ya Lusophone ndi Mbusa Dr. Sueia, ma Ds ndi abusa awo onse.

Mupempherere mfundo komanso ndondomeko izi mu zigawo zina zazikulu: kuoneka kwa kupezeka kwa Mulungu, uthenga, kupanga ophunzira, chiyero, kutukula mpingo, zigawo ndi atsogoleri Ake, kukula kwa utumiki koyenera, kudzipereka pa utumiki kwa unsembe, kutsitsimuka kwa Mzimu Woyera.

Tsopano, ndikuiatana magulu ang’onoang’ono kuti apemphere kwa mphindi ziwiri. Pamene kuyimba kwayambika, chonde tsekani nthawi yanu yopemphera.

Imbani: Mulungu wopanda chiyambi kapena nyimbo ina

Mtsogoleri wachitatu: Tikupitiliza kupempherera akulu azigawo zina zazikulu muno mu Africa ndipo awa ndi apakatikati pa Africa komanso kuzambwe kwa Africa. Iwowa ndi Mbusa Chanshi Chanda komanso Mbusa Mark Louw wa Kuzambwe kwa Africa.

Tonse tiime Tiwerenge Mateyu 24:14 limodzi pakanema: “Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa padziko lonse lapansi, ukhale umboni kwa anthu amitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimaliziro (Mateyu 24:14).

Ndikulimbikitsa anthu amene ali kudzanja langa lamanja, kuti apempherere Mbusa Chanshi Chanda ndi ma DS komanso Abusa awo, ndipo akumanzere apempherere Mbusa Mark Louw chigawo chake ma DS, Abusa awo.

Pemphererani zina mwa mfundo izi mu zigawo zawo: kupezeka kwa Mulungu, uthenga wabwino, kusula ophunzira, chiyero, kutukula mpingo, zigawo zazing’ono ndi atsogoleli awo, kukula kwa utumiki koona, udindo wodzipereka, komanso kutsitsimuka kwa uzimu. Pemphererani kwa mphindi ziwiri ndipo mutseke kuimba kukangoyambika.

Imbani: Fuulani kwa Ambuye kapena nyimbo ina

Mtsogoleli wa chinayi: Titseka ndi pemphero poikiza mmanja mwa Ambuye Chigawo Chakummwera kwa Africa komanso ofesi yampingo wonse mu Africa (Africa Region). A Strategy Coordinator a South Field ndi Mbusa Collin Elliott. A Regional Director, muno mu Africa ndi Dr Filimao Chambo. Khalani mumagulu ndi kupempherera limodzi.

Ndipemphe lwo amene ali kudzanja langa lamanja kupempherera Chigawo Chakummwera cha Africa ndi Mbusa, ma DS awo komanso Abusa awo onse

Anthu adzanja langa lakumanzere, akhale mumagulu ndikupempherera ofesi ya mpingo ku Africa kuno komanso Dr. Filimao Chambo ndi gulu lawo.

Kenaka, mupempherere a Ds adera lanu, abusa onse komanso abusa ampingo wanu.

Pemphererani mitu iyi: kuoneka kwa kupezeka kwa Mulungu, uthenga wabwino, kupanga ophunzira, chiyero, kutukuka kwa mpingo, zigawo zones ndi atsogoleli, kukula kwa utumiki, udindo waunsembe, komanso kukula muuzimu.

Tsopano, itanani anthu apemphere kwa mphindi ziwiri. Nyimbo zikayamba, tsekani ndi pemphero.

Nyimbo ikatha, muli ndi ufulu kukhala ndi nthawi yachiyanjano kapena chidyerano pankhomalilo. Mukhalenso ndi khumbo la cholinga cha utumiki wathu chimene ndikupanga ophunzira ofanana ndi Yesu Khristu padziko lonse kuyambira ku Africa kuno.

Imbani: Akulamulira kapena nyimbo ina

Mtsogoleri wachipembedzo: Nyimbo yoyamika Mulungu

Kusalira Kutsitsimuka pa Chiyero

“Patulani tsiku losala; lalikirani masonkhano oletsa; sonkhanitsani akulu akulu, ndi onse okhala mdziko, kunyumba ya Yehova Mulungu wanu; nimupfuulire kwa Yehova”

Yoweli 1:14

Kodi Kusala Ndi Chiyani?

Kusala ndi kudya modzimana pakufuna.

Kusala ndi dongosolo lauzimu limene lidayambika muchipangano chakale. Kusala koyamba mu Buku Lopatulika kumene kudachitika tikukuona pa Eksodo 34:27-28, “Ndipo Yehova anati kwa Mose, ‘ulembere mau awa, pakuti monga mwa mawu awa ndapangana ndi lwe ndi Israeli.’ Ndipo anakhala pomwep ndi Yehova masiku makumi anayi, usana ndi usiku, sanadya mkate kapena kumwa madzi. Ndipo analemba pamagomewo mawu a panganolo, mawu khumiwo.”

Yesu adasala masiku makumi anayi mchipululu ali pafupi kukayesedwa ndi satana (Mateyu 4:1-11), ndipo adaonetsera mmene tingagonjetsere mayesero a satana pamene tidziwa, kulandira ndi kukhulupirira mau a Mulungu.

Palinso mavesi Ena amene amanena zakusala kudya ndipo ndi awa, Luka 2:36-37, Machitidwe a Atumwi 13:1-3, ndi Machitidwe 14:23.

Kusala kwa uzimu kutanthauza kuika padera ntchito zina komanso kuchepesa zakudya zimene timadya ndi cholinga chokhudzidwa ndi pemphero komanso zinthu za uzimu.

Ndi nthawi yodalira Mulungu pa mphamvu, kuphweka kwa maganizo ndi mtima, ndi njira; komanso nthawi yakuyanjana naye mwapadera.

Pali magawo atatu akusala odziwikiratu ndipo ndi awa: *kusala kodziwikiratu*, kusala chakudya kwakanthawi ndipo kumakhala kumwa madzi ochepa kapena chakudya chochepa ndipo kwina ndi kwakuti chakudya ndi madzi sizimakhlapo.³

Pambali pazakudya kusala kwina kumachitika posala zinthu zotikondweretsa monga mpira, zoimbaimba ngakhalenso kusala kukhalira malo amodzi monga banja ndi cholinga chofunafuna nkhope ya Ambuye.

- Kusala kuzitsagana ndi kulapa, komanso kuwerenga mawu a Mulungu. (Masalimo 51:1-13, Masalimo 119:9-16)
- Kudzichepetsa ndikofunika posala (Yesaya 58:5)
- Kuyenera kuchitika moona ndi molemekeza Mulungu (Mateyu 6:16-18).
- Kusala kuchitike ndi mtima wokondwera komanso woyamika (Mateyu 6:17-18)
- Kusala kuyenera kutsagana ndi mtima womvera Mulungu (Yesaya 58)

³ Elwell, W. A., & Comfort, P. W. (2001). *Tyndale Bible dictionary*.

- Tiyenera kukumana ndi zosowa za Ena pamene tikusala kudya ndi kupemphera (Yesaya 58:6-7)

Zinthu Zina Zoyenera Kuchita Posala Kudya

- Ena amaona kuti nzosavuta kusala poyamba kuchepetsa kadyedwe pang'onopang'ono,
- Anthu amatenda monga a shuga ayenera kukafunsa kwa adotolo asadayambe kusala
- Ana ngathe kuphunzira kusala poyamba kusala maswiti ndi zina kaya zidole
- Mukhale ndi nthawi yowerenga mau panokha komanso pagulu panthawi yosala kuti mulimbikitsane
- Pakutha pakusala mungathe kukhala ndi nthawi yomasula limodzi pachakudya kapena mgonero.
- Simuyenera kudya kwambiri nthawi yomasula chifukwa zingathe kukuvutani pakusala
- “Kulandira dalitso loyenera pakusala, limafuna kudzipereka. Kukhala ndi nthawi yachete patsiku yolumikizana ndi Mulungu ndi zofunika zedi. Mukhale ndi nthawi yofuna nkhope ya Mulungu ngakhale nthawi imene zinthu sizili bwino. Mukhale ndi nthawi yowerenga mau nthawi imene mukanakhala mukudya chakudya chanu. Lingalirani Mulungu mukadzuka usiku ndipo muimbe nyimbo zakumtamanda”. (Dr Bill Bright, Mlozo wanu wa kusala kudya ndikupemphera)

Mlozo wa kupemphera ndi kusala kudya wakonzedwa ndi Mbusa Samantha Chambo, Africa Regional NMI Coordinator

Kukondwerera Pemphero Lachiyero ndi Mfundo Zakusala ndi Zilinganizo zake

Lolemba	Lachiwiri	Lachitatu	Lachinayi	Lachisanu	Loweruka	Lamulungu
20 Mfundo yapemphero lasabata	21 Febuluwale	Lachitatu laphulusa Lachitatu 22 Gulu lapemphero laling'ono	23	24	25	26 Mwambo wokhazikitsa Kukondwerera chiyero
27 Africa South Field Africa Regional Office Gulu: Amayi	28	29 Pemphero la gulu laling'ono	1 March	2 Mapemphero a usiku ampingo wonse	3	4 Mwambo wopembedza ndikuyamika
5 Africa Middle Field Likulu lampingo Gulu: Amuna	6	7 Pemphero lagulu laling'ono	8	9	10 Msonkhano wapemphero	11
12 Africa Lusophone Field Africa Central Field Gulu: Anyamata okulirapo	13	14 Pemphero lagulu laling'ono	15	16 Mapemphero a usiku ampingo wonse	17 Pemphero loyendayenda	18
19 Horn of Africa Field	20	21 Pemphero la gulu la	22	23	24	25

Africa West Field Gulu: Achinyamata		ling'ono				
26 Africa East Field HIV/AIDS ndi anthu anjala Gulu: Ana	27	28 Pemphero la gulu laling'ono	29	30 Kuyenda mpemphero	31	1 Epulo
2 Kutsanulidwaka Mzimu Woyera mu aafirika ndi dziko lonse Gulu: Mpingowonse	3	4 Pemphero la gulu laling'ono	5	Lachisanu loyera 6 Mbindikiro wampemphero	7	Lamulungu loyera 8 Msonkano woyamika!

CHICHEWA